

KUPANGA BOKASHI

Ndondomeko yogwiritsa nchito alimi ang'onoang'ono

Tsatanetsatane wa njira yopangila Bokashi



Sitepi 1. Sankhani malo omwe ali ochinjiziridwa ku mvula, mkuntho ndiponso dzuwa.



Sitepi 2. Yambani mwa kuyala zowuma pansi, ikani ndowe pamwamba pa zowuma ndiponso muyale dothi pamwamba pa ndowe. Pamwamba pa dothi, tayalani malasha ndipondo gaga. Kumbukani kuti unyinjwa wa zopangalazi poyala ulibe nchito kwambiiri chifukwa pomaliza zonsezi zisasakanizidwa.



Sitepi 3. Tasakanizani molasi ndi chotupisa m'madzi okwanira ma lita 5 ndipo wazani pamwamba pa zopangila mwayalazo.



Sitepi 4. Chitaninso sitepi 2 ndi 3 mpaka mutamaliza zopangila zonse. Mutamaliza kuyala zonse zofunika, Bokashi siifunika kupitilira utali wa ma mita 1.5.



Sitepi 5. Pindimulani Bokashi wanu kuti zonse mwayala zisakanizike bwino bwino.



Sitepi 6. Wazani madzi ku Bokashi pamene mukupindimula. Osawaza madzi ochuluka. Pindimulani Bokashi wanu katatu kapena kanayi kuti zonse zisakanizike bwino bwino.



Sitepi 7. Mutamaliza ku kusakaniza Bokashi, tengani dzanja limodzi la Bokashi ndipo finyani kuti muone ngati mwaika madzi ambiri kapena ochepe. Ngati madzi atuluka pakati pa tumbombo ndiye kuti mwaika madzi ambiri. Ngatinso Bokashi sapombana ngati soseji m'manja mutafinya, ndiye kuti madzi ndi aang'ono. Ngati madzi achuluka, pindimulani ndi kuonjezako dothi ku Bokashi. Ngati madzi ndi ochepe, pindimulani ndi kuwaza madzi pamene mukusakaniza Bokashi. Kumbukani kuti madzi amaikidwa chabe pa tsiku lopanga Bokashi.



Sitepi 8. **Kusamala Bokasi** – Ngati mungaike dzanja lanu mu Bokashi kwa ma sekondi 10 osamva kupsa, ndiye kuti bokashi wanu ali bwino. Ichi chitanthauza kuti Bokashi wanu ndi wakupsa ma digiri 55. Pindimulani ndi kusakaniza Bokashi wanu kawiri pa tsiku kwa masiku anayi oyamba m'mawa ndi m'madzulo. Ngati mutaika dzanja lanu mu Bokashi mwanwa kutentha kwambiri mufunika kufupikisa utali wa Bokashi wanu kuti asamapsa kwambiri chifukwa azaonongeka.



Sitepi 9. Pindimulani Bokashi wanu kamodzi pa siku kuyambira tsiku la chisanu mpaka Bokashi ataleka kupsa nkulingana ndi mphopo yozungulira. Bokashi wanu azakhala atapsa pa siku la 12 kufika 15. Pamene pamukhoza kugwiritsa nchito Bokashi.

Gwiritsani nchito Bokashi msanga msanga atapsa chifukwa ndipo pamene amakhala ndi mphanvu kwambiri. Si kwabwino kusunga Bokashi kwa nthawi yaitali kupyola pa mwezi umodzi.

Kodi Bokashi ndi chiyani?

Bokashi ndi fataleza wa chilengedwe womwe umapangidwa mwa kusalola kuti zogwiritsa nchito popanga zisasilizike kuwola.

Ndi zotani zimene zimafunikira popanga Bokashi?

Kuti Bokashi ipangidwe, pafunika izi:

- ▶ Masaka 7 a mpimo wa ma kilo 50 a ndowe zomwe mupezeka zakudya za mbewu ndiponso tizilombo tosaoneka ndi maso. Mukhoza kugwiritsa nchito ndowe zilizonse, koma mukasakaniza ndowe, zimagwira nchito mwampamvu ndiponso ndowe zifunika kukhala zowuma.
- ▶ Masaka 7 a mpimo wa ma kilo 50 a zowuma zimene ziwola monga zokhalira ku chimanga, mamba a mpunga, mayani owuma ndi ufa wochoka ku matabwa. Zowuma zimenezi zimagwira nchito bwino zikakhala zosakaniza ndiponso zifunika kukhala tuzibenthu tating'oting'ono kuti tuwole msanga.
- ▶ Masaka 5 a mpimo wa ma kilo 50 a dothi lapa chulu olo la munsu mwa mitengo. Dothi ndi lofunika kwambiri mu Bokashi chifukwa ndimo mupezeka tulombo tosaoka ndi maso.
- ▶ Saka limodzi la malasha osinjiwa a mpimo wa ma kilo 50 ngati nkotheke kulipeza. Malasha amapangitsa kuti tulombo tosaoneka ndi maso tugwire bwino nchito.
- ▶ Saka limodzi la mpimo wa ma kilo 50 a gaga wa chimanga, mpunga kapena tirigu. Gaga ndi chakudya cha bwino kwambiri cha tulombo tosaoneka ndi maso.
- ▶ Ma lita 5 a molasi. Molasi imapatsa mphanvu ku tulombo tosaoneka ndi maso kuti tugwire bwino nchito. Ngati molasi palibe, mungagwiritse nchito shuga mwa kusungunula ma kilo awiri mu madzi. Koma molasi umagwira nchito bwino ndiponso ndi wochipa.
- ▶ 500g wa chotupisa (yeast) kuti tulombo tusaoneka ndi maso tubalane mwamsanga.
- ▶ Mwala wogaya kapena ufa wa mafupa oocha. Ngati palibe izi, gwiritsani nchito choto.
- ▶ Madzi osaikidwa mankhwala aliwonse ngakhale kolorini yomwe.

Chonde kumbukani kuti: mipimo yaikidwai ndi zitsanzo chabe. Munthu angathe ku chinja zopangira Bokashi kulingana ndi zofunika zimene ali nazo.



Promotion of agroforestry supported by:



by decision of the German Bundestag